Tape No B4163 N.Z. 12/94

KUYALA MAZIKO 4

Chikhulupiriro ndi Ntchito

Ndipo usiku uno cholengeza chathu chiri chogwirizana mwachindunji ndi mutu wa zomwe ndikhale ndikulankhula. Zatengedwa kuchokera ku Aefeso 2:8–10. Aefeso 2:8–10.

Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro, ndipo ichi chosachokera kwa inu chiri mphatso ya Mulungu, chosachokera ku ntchito, kuti adzitamandire munthu aliyense. Pakuti ife ndife chipango chake, olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo.

Tsopano ndipitirira ndi mutu womwe tinayamba mu gawo lapitalo, ichi ndicho, kufufuza ziphunzitso zisanu ndi chimodzi za maziko a chiphunzitso a chikhulupiriro cha chikhristu zomwe zalembedwa mu Ahebri 6:1 ndi 2.

Ndingozibwerezanso.

- **Kutembenuka mtima kusiyana nazo ntchito zakufa,**
- **chikhulupiriro cha pa Mulungu,**
- **chiphunzitso cha maubatizo,**
- **kuika manja,**
- **kuuka kwa akufa ndi chiweruzo chosatha.**
- Mu phunziro lathu lapita ndimalankhula za "**kudzera mu kutembenuka mtima kupita ku chikhulupiriro**.

"Ndinalankhula za kutembenuka mtima ndipo ndinayamba kulankhula za chikhulupiriro. Ndifuna ndipitirire madzulo ano kulankhula za chikhulupiriro ndi ntchito; mau awiri omwe amagwiritsidwa ntchito kwambiri mu Chipangano Chatsopano ndipo komatu ndi zodabwitsa momwe ambiri a anthu a Mulungu sakhala ndi chidziwitso chomveka bwino cha ubale pakati pa ntchito ndi chikhulupiriro.

Ndinene kuti mwa chikhulupiriro tikutanthauza za chomwe tikhulupirira, mwa ntchito tikutanthauza zomwe tichita. Kodi ubale woyera pakati pa zomwe tikhulupirira ndi zomwe tichite wotani?

Ndifuna ndiyambe poyamba ndi kungofotokoza mwa chidule za uthenga. Ambiri a ife timagwiritsa ntchito gawo la chiganizo lakuti "uthengawo" ndipo timalankhula za iwo ngati ndi chinthu chomwe tichidziwa bwino kwambiri za chomwe titanthauza. Mu zeni zeni, ndiganiza anthu ambiri amalankhula za uthengawo ndipo sali odziwa za chomwe uthengawo uli. Ukufotokozedwa bwino ndi Paulo mu 1 Akorinto 15:1–5, 1 Akorinto 15:1-5.

Ndipo ndikudziwitsani, abale, uthenga wabwino umene ndinakulalikirani inu, umenenso munalandira, umenenso muimamo, umenenso mupulumutsidwa nao ngati muugwiritsa monga momwe ndinalalikira kwa inu, simunakhulupirira chabe.

Ndipo kenaka Paulo akupitirira kufotokoza za uthengawo. Ndipo uthengawo umafotokozedwa mu magawo atatu a zoonadi za mbiri, suli ovuta.

Pakuti ndinalandira, kuti Khristu anafera zoipa zathu monga mwa Malembo.

Kotero uthenga uli ndi zinthu zitatu zambiri: Khristu anafera machimo athu.

Anaikidwa m'manda ndipo anaukisidwa kwa akufa pa tsiku la chitatu. Ndipo pamene zinthu zitatu sizinanenedwe, uthenga sunalalikidwe, pali ambiri a iwo otchedwa olalikira uthenga umene sukhala ndi uthenga weniweni. Izi ndi zinthu zitatu zazikulu zomwe tiyenera kugwiritsa: Khristu anafera zochimwa zathu, Anaikidwa m'manda ndipo anaikisidwa tsiku la chitatu.

Ndipo chinthu choyamba chotsimikizira ulamuliro si mboni yoona ndi maso yomwe idamuona iye atauka kwa akufa, koma malemba. Uwu ndiye ulamuliro wotsiriza. Paulo akulankhula izi kawiri, "monga mwa Malemba," ndipo akupitirira kunena za anthu ena omwe anali mboni za kuukanso kwa akufa kwake. Koma lingalirani ichi m'moyo wanu kuti ulamuliro womaliza mu zinthu zonse zonse zokhudza chikhulupiriro ndi Malemba.

Tsopano, Paulo akupitirira kufotokoza kuti ngati tilandira zinthu zophekazi ndi chikhulupiriro, popanda ntchito, popanda chimene tichita, chilungamo chidzaikidwa pa ife. Tidzayesedwa olungama. Ndi zofunika kwambiri kuona kuti Paulo akunena kuti sizimene tichita koma zimene tikhulupirira. Si mwa ntchito koma mwa chikhulupiriro. Akupitirira kunena ku Aroma mutu 4 kukamba za phunziro lomwe tingaphunzire kuchokera kwa Abrahamu pakuti ikunena kuti Abrahamu anali ndi chilungamo chinaperekedwa kwa iye mwa chikhulupiriro. Paul kenaka akuyamba kukamba za phunziro kuchokera ku izi. Akunena ku Aroma 4:

Tsopano kwa iye yemwe agwira ntchito, malipiro sawerengedwa monga chisomo koma ngongole. Ngati mukugwira ntchito wina ndi kulandira malipiro anu, ichi si chisomo, ndi china simomwe timapezera chilungamo. Simwa ntchito zathu, si chinthu chomwe tachigwirira ntchito.

Ndipo akupitira kunena mfundo yodabwitsa pa zonse, ndipo ndimawauza anthu kuti ngati musanadabwitsidwepo ndi zomwe mukuwerenga mu Baibulo, chifukwa limakhala ndi zinthu zodabwitsa kuposa mtunda zonse. Paulo akupitirira kunena mu Aroma 4:5

Koma kwa iye amene sachita, koma akhulupirira iye amene ayesa osapembedza ngati olungama, chikhulupiriro chake chiwerengedwa chilungamo.

Kotero, ngati mufuna chikhulupiriro chanu chiwerengedwe chilungamo, kodi chinthu choyamba choyenera kuchita ndi chiyani? Siyani kugwira ntchito. "kwa iye yemwe sachita." Pamene inu muganiza kuti mungathe kuchipeza mwa zomwe muchita, simudzachilandira. Ichi ndi chinthu cholimba kwambiri kwa anthu achipembedzo. Tinazolowera kwambiri ganizo lakuti tiyenera kuchita kanthu kena kuti tilandire kukondera kwa Mulungu. Kukondera sikumapezeka mwa

kuchita china chake. Chisomo simungachipeze pochita china chake. Pakufotokozera ndiye kuti sangachipeze mwa kuchita china chake. Ndipo kotero, chinthu choyamba chomwe muyenera kuchita ngati mufuna muyesedwe olungama ndi Mulungu ndi kusiya kuyesa. Musagwire ntchito. Iyi ndiye mfundo yoyambira kwa anthu ambiri, koma Baibulo ndilo bukhu lodabwitsa koposaposatu kupitirira momwe ambiri a ife tidziwira.

Kodi pali ubale wotani pakati pa chikhulupiriro ndi ntchito? Si chifukwa chakuti ntchito ziri zosafunika, ndi ndondomeko yomwe tifikira. Rute ndi ine tinatenga ndime kuchokera ku Aefeso 2 yomwe ndibwererakonso. Aefeso 2:8-10.

Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo chakuchita mwa chikhulupiriro ndipo ichi chosachokera kwa inu chiri mphatso ya Mulungu…….

Sitinganyade chifukwa cha choonadi chakuti tinali ndi chikhulupiriro chifukwa Mulungu anatipatsa ife. Si chinthu chomwe chingapangidwe kuchokera mwa ife tokha.

Ndipo kenaka ikuti:

Chosachokera ku ntchito, kuti asazitamandire munthu ali yense.

Ndipo malo ambiri omwe akulankhula za anthu omwe akhulupirira kuti ayesedwa olungama omwe akhulupirira kuti ayesedwa olungamo mwa ntchito zao, Paulo akuti ai, kuti asadzitamandire. Mukuona, chipembedzo cha ntchito chimabweretsa kunyada kwa umunthu. Ndipo kunyada ndiko maziko a chimo lalikulu la maziko. Kotero, Mulungu wakhazikitsa njira ya kukhalira olungama yomwe siimabweretsa kunyada kwathu.

Ngati mutalingalira anthu omwe ali ndi zipembedzo zosamvetsetseka, ndipo kunena ngakhale umodzi wa iyo chifukwa sindifuna kuoneka kuti ndikulimbana ndi china chake, koma pogonera pake ndi pakuti, momwe kuvuta kwa zipembedzo zao ziri ndi momwe kunyada kwao kuliri. Akuchita chinthu china molimbika ndi chovuta: kusala, kupereka nsembe ndi zina zotero. Izi zimayambitsa kunyada. Mulungu amakaniza odzikuza koma amapereka chisomo kwa odzichepesa. Kotero Mulungu wapanga njira yopezekera olungama ndi iye yomwe siibweretsa kunyada.

Sindikudziwa ngati munazindikira ichi, koma kwambiri tiyeni tikambe za a khristu. Akhristu omwe ali a lamulo, okhazikika pa malamulo, kawirikawiri amakhala anthu opanda chikondi, kodi izi munaziona? Ngati mungapite kwa iwo pofuna chikondi simungalandire chokwanira. Ndipotu, kutsata malamulo ndi chikondi ndi zinthu ziwiri zotsutsana. Kotero, tiyenera nthawi zonse kukhala a tcheru motsutsa china chiri chonse chomwe chimabweretsa kunyada. Ndipo chipembedzo chimabweretsa kunyada. Ngati chiri chipembedzo chopanda chisomo cha Mulungu chimabweretsa kunyada kwathu.

Koma, pali malo a ntchito. Siziri zopanda ntchito, ndi zongofunika kungoziika mu ndondomeko yoyenera. Aefeso 2:10, ikunena momveka bwino monga momwe ndidziwira.

Pakuti ife ndife chipango chake, olengedwa mwa Khristu Yesu, kuchita ntchito zabwino, zimene Mulungu anazipangiratu, kuti tikayende m'menemo.

Kotero pomwe Mulungu anatilenga atsopano mwa Khristu, ndipo Baibulo linena kuti ngati wina ali mwa Khristu ali wolengedwa kwatsopano, kenaka Mulungu ali ndi ntchito zokonzedweratu za wolengedwa kwatsopano. Koma umunthu wakale sungayende mu ntchito zabwino zimene Mulungu wazikonzeratu. Ndiye muyenera kulengedwa kwa tsopano mwa chikhulupiriro musanayambe kuyenda mu ntchito zabwino. Ndiye ntchito zabwinozi zidzakhala zofunika kwambiri. Koma muyenera kupeza ndondomeko yoyenera. Poyamba pa zonse, kulengedwa kwatsopano kudzera mu chikhulupiriro; kenaka ntchito zabwino zomwe Mulungu anazipangiratu ife.

Sindikudziwa ngati munazindikira, simusowekera kuchitapo kanthu pa zomwe Mulungu ayenera kuchita, ngati mwalengedwa kwatsopano mwa Khristu, chifukwa Mulungu wazichita kale. Chomwe muyenera kuchita ndikupeza ntchito zomwe Mulungu anakukonzerani kale. Musayesere kudzipangira nokha chikonzero cha moyo wanu, fufuzani chikonzero chomwe Mulungu ali nacho pa inu. Nthawi zambiri ndi zosiyana ku zomwe ife tiyembekezera.

Ndikupatseni chitsanzo cha pafupi kuchokera ku zondichitikira. Ndinali mwana m'modzi yekhayo, ndinalibe abale kapena alongo. Ndinakulira masukulu ogonera komweko kuyambira pa zaka 9 mpaka 25. Sindimakumana ndi atsikana kawirikawiri ngakhale kuti ndinali ndi abwenzi achitsikana ochepa. Ndipotu atsikana anali chinthu chosamvetseka kotero ine sindimadziwa momwe ndikadayanjanirana nawo. Koma pomwe Mulungu anandiitana, ndinakwatira mkazi yemwe anali ndi nyumba yosamalira ana ndipo tsiku lomwe ndinamukwatira ndinakhala tate wa atsikana oleredwa asanu ndi atatu. Mwaona, simukadaganiza kuti ichi chinali chinthu chomuyenera Derek Prince. Ndikadakhala kuti ndinapanga chikonzero cha moyo wanga zimenezi sindikanazichita ndikomwe. Koma ndi ntchito zabwino zomwe Mulungu anazikonzeratu kuti ine ndiyendemo. Ndimapeza kukhutisidwa, ngakhale ndalephera mu njira zambiri, podziwa ichi makamaka ndayenda mu ntchito zabwino zomwe Mulungu anazikonzeratu kwa ine.

Tsopano, tiyeni tifike ku kofotokozera pang'ono ndipo pamenepa ndipo tisowa kuganiza bwinobwino. Zoona zake, musowekera kuganiza bwino nthawi zonse! Ndi angati omwe mungandivomereze? Chabwino tsopano, tisowekera kukambirana mwachidule za chikhalidwe cha chisomo. Chisomo ndi liu labwino koma nthawi zambiri limagwiritsidwa molakwika. Ndinkalalikira nthawi ina mu tchalitchi china ndipo ndinanena, Zoona zake ndi zakuti mipingo yomwe imadziwatchula "chisomo" ndi mipingo yomwe imadziwa pang'ono za chisomo." Ndipo ndinazindikira ku choona chakuti ndimalalikira mu mpingo wa umodzi wa iyo! Ngakhale zinali choncho, izi zikhalabe zoona. Anthu ambiri omwe amagwiritsa ntchito mau akuti chisomo alibe chidziwitso china chiri chonse zomwe litanthauzadi. Tanthauzo lenileni la chisomo ndilo chokoma kuona, ndiko kukongola. Ndipo uku ndi kukongola komwe Mulungu amapereka, kwa ife chifukwa takhulupirira mwa iye. Amatipanga kukhala okongola kudzera mu chisomo chake.

Ndipo kenaka Paulo akuti – apa ndipo pali gawo lofunika kwambiri – Aroma 11:6.

Koma ngati kuli ndi chisomo, sikulinso ndi ntchito ai; ndipo pakanda kutero, chisomo sichikhalanso chisomo.

Mu kulankhula kwina, mu chilankhulo changa, simungagwirire ntchito chisomo. Ichi ndi chinthu chotipangitsa kudzichepetsa kwa ambiri a ife. Tiyenera kudalira pa chisomo chake, sitingagwirire ntchito. Palibe chomwe tingachite kuti tipeze chisomo cha Mulungu. Koma ndi chisomo tinapulumutsidwa kudzera mwa chikhulupiriro. Ndipo pomwe inu mukungosangalatsidwa ndi choona chakuti muli ndi chikhulupiriro, kumbukirani Paulo akupitirira kulankhula kuti:

…...ichi chosachokera kwa ife, chiri mphatso ya Mulungu.

Mulibe china chiri chonse chakuti munyadire ngati munapulumutsidwa ndi chikhulupiriro. Mulungu anachita ichi kuti akutetezeni ku tchimo lalikulu pa onse, lomwe ndi kunyada.

Ndifuna kulingalira za ubale pakati pa chikhulupiriro ndi ntchito, chomwe tikhulupirira ndi chomwe tichita. Ndipo monga momwe ndidziwira, zonse zomwe ndinene zitengedwa ku Chipangano Chatsopano komatu kwa ambiri a inu zikhala zodabwitsa ngakhalenso zodzidzimutsa. Ndinapeza ichi pakungolalikira uthenga wosavuta wa Chipangano Chatsopano wa chipulumutso ndi chisomo ndi chodabwitsa kwa Akhristu ambiri ovomelezadi khristu.

Ndikumbukira kamodzi kulankhula ku msonkhano wofanana ndi uno. “Indetu, Chikhristu si ndondomeko ya malamulo; Ndipo kenaka ndinayang’ana anthu awo ndipo anadabwitsidwa. Ndiganiza akadakhala odabwitsidwa pang’ono ndikadakhala kuti ndinanena kuti,” “Mulungu ndi wakufa” Ganizo lawo pa chikhristu linali ndondomeko ya malamulo; mwinanso inu mumaganiza choncho. Ndikufuna ndikuuzeni kuti chikhristu si ndondomeko ya malamulo. simungachipeze ndi malamulo.

Tiyeni tione zomwe Paulo anena ku Aroma 3:20. Mutu wa bukhu la Aroma, ndiwonso, chilungamo. Iyi ndiye nkhani ya paphata ya Aroma, iri momwe tingakhalire olungama pamaso pa Mulungu? Zaka zambirimbiri zapitazo, Yobu anafuula mu ululu mu Yobu 9:2.

“Koma munthu adzakhala wolungama bwanji kwa Mulungu?

Ndipo abwenzi ake a chipembedzo ananyoza mfundo yakuti munthu angathe kukhala wolungama pamaso pa Mulungu. Koma Mulungu anamva kulira uko ndipo zaka zambirimbiri pambuyo pake kudzera mu kalata ya ku Aroma. Anayankha funsoli.

“Koma munthu adzakhala wolungama bwanji kwa Mulungu? Ndipo si mwakusunga malamulo.

Ku Aroma 3:20 paulo akuti:

Chifukwa kuti pamaso pake palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo (iri si thupi la munthu) chifukwa uchimo udziwika ndi chilamulo.

Tsopano ndiwerenga mamasulidwe awa omwe ali mu mamasulidwe a K.J.V.,(la Chingerezi). Mu mamasulidwe N.I.V limakambanso chimodzimodzi. Onse awiri kuwaika pamodzi ndi omwe sakupezeka pamenepa. Ndinaphunzira chi Griki, kuyambira pomwe ndinali ndi zaka khumi. Ndiri ndi chitsimikizo pa zomwe ndi kunena. Amaika gawo la chiganizo "lamulo" kawiri. Lamulolo. Paulo sakunena choncho. Akuti.

"Chifukwa chake mwa ntchito za lamulo palibe thupi lomwe lidzapulumutsidwa, chifukwa mwa lamulo tchimo limadziwika.

Mukunena, "chabwino kodi cholinga cha lamulo chinali chotani?" Cholinga cha lamulo chinali chotani? Cholinga cha lamulo chinali chomwe Mulungu amagwiritsa ntchito kuvumbulutsira poyera mavuto anu, kuvumbulutsira kuti muli ndi vuto lomwe ndi tchimo. Lamulo lingathe kudziwitsa vuto lanu koma silingalikonze. Lingathe kukonzedwa ndi chisomo. Kotero musowa lamulo kuti likutengereni inu pa malo pomwe mungathe kuona chosowa chanu cha chisomo, ichi ndiye cholinga chake.

Yakobo akunena mu mutu 2 wa kalata yake, Yakobo 2:10:11.

Pakuti amene ali yense angasunge malamulo onse (apa akukamba za lamulo la Mose) koma akakhumudwa pa limodzi, iyeyu wachimwira onse. Pakuti iye wakuti, Usachite chigololo anatinso, Usaphe. Ndipo ukapanda kuchita chigololo, koma ukapha wakhala olakwira lamulo.

Mukuona zomwe Yakobo akulankhula? Muyenera kuti mukusunga malamulo onse kapena sukusunga lamulo. Kusunga gawo lalikulu la lamulo sikusunga lamulo. Lamulo ndi chilamulo chonse. Muzenizeni, Palibe wina wa ife kwina kulikonse pafupifupi onse. AYuda a Orthodox ali ndi malamulo 613 omwe oyenera kuwatsatira. Ndipo mwamseri onse adzavomera kwa inu kuti samatsatira ena ali wonse koposa 32. Palibe wina aliyense yemwe ali ndi moyo pansi pano yemwe amasunga malamulo onse a Mose. Palibe yemwe adakwaniritsapo koma munthu m'modzi. Mudziwa dzina lake, Yesu, zoona. Amakhoza kunena kwa anthu awo a mu nthawi yake ya pansi pano, "Ndani wa inu anganditsutse ine za tchimo?" Sankamuyankha iye. Ndi yekhayo yemwe adasunga malamulo bwino lomwe. Inu ndiine sitingathe kukwaniritsa.

Ndinapeza pomwe ndinali mu gulu la nkhondo la ku Mangalande ndipo ndinapulumutsidwa ndi kuyamba kwa anthu zokhudza kupulumutsidwa, anayamba kuganiza mogwirizana ndi chipembedzo osati ndi chipulumutso. Ndimakhoza kupeza, kunena monga anthu onse, wina aliyense wa iwowa akadakhodza kulemba ndondomeko yaing'ono ya omwe amasunga. Ichi chinali chilungamo chake. Chimakonzedwa kuti chigwirizane ndi momwe chiri cholakwika chomwe amachita samachiphatikiza ku mudandaula wao. Ndinaona kuti umu ndi momwe maganizo a munthu amaganizira. Ndiri olungama pakusunga gulu la malamulo. Ai, simukhala olungama. Mukadakhoza kukhala pokhapo mukadasunga lamulo lonse koma simusunga, palibenso amasunga. Kotero sumungathe kunena, "Ndimasunga ambiri a malamulo ndipo ichi ndicho chisoweka," chifukwa lamulo ndi mchitidwe umodzi. Mumausunga kapena simusunga. Mukadasunga lamulo lonse, Mulungu adakuyesani wolungama. Koma, simungathe. Kotero, ndinu wotsekeka ku cholowa m'malo mwake chomwe ndi chisomo. China chake chomwe simungachigwirire ntchito.

Ndaisonyeza kale, ndipo ndikubwereraku mfundo iyi, ku Aroma 3:20:

Chifukwa kuti pamaso pake palibe munthu adzayesedwa wolungama ndi ntchito za lamulo.

Osadzayesa kupeza chilungamo ndi Mulungu pakusunga ndondomeko ya malamulo. Ichi ndi chomwe zikutanthauza, chifukwa mumalephera. Ngati malamulo anu ali oona, simungathe kuwasunga. Ngati malamulo anu ali olakwika, simumayesedwa olungama pa kusunga malamulo. kodi mukumvetsa?

Tsopano tiyeni tipitirire. Chinthu chotsatira chomwe ndifuna kunena, ndipo apa ndi pomwe anthu amayamba kudabwitsika, kodi chilamulo ndi chisomo zimatheka kukhalira pamodzi. Simungapindule kuchokera mu zonsezi ziyenera kukhala chimodzi kapena chinzake

Ngati mungapitirire ku Aroma 6 kufikira ndime 14, ikuti:

Pakuti uchimo udzachita ufumu pa inu; popeza simuli a lamulo koma a chisomo.

Kotero izi ndizo ziwiri zomwe sizingayendere limodzi, ndi chimodzi kapena chinzake. Mungathe kukhala pansi pa lamulo kapena pansi pa chisomo koma simungakhale pansi pa ziwirizi nthawi imodzi. Ndipo ngati muli chilamulo ndiye simuli pansi pa chisomo, ndipo ngati muli pansi pa chisomo simuli pansi pa chilamulo.

Zolumikizitsa zomwe Paulo anena ndi zapamwamba kuzifikira. Akunena kuti tchimo silidzakhala ndi ulamuliro pa inu, simuli a chilamulo koma achisomo. Zolumikizitsa (zoyanjanitsa) ndi zakuti ngati muli pansi pa lamulo, uchimo udzakhala ndi ulamuliro pa inu. Njira yokhayo yothawira kukhala pansi pa ulamuliro wa uchimo ndiko kusiya kuyesa kusunga chilamulo ndi kudzipereka nokha ku chisomo cha Mulungu. Ndinakuuzani kuti izi zikhoza kukhala zodzidzimutsa. Ndikuona kuti ena inu mukusonyeza kuti muli adzidzimutsidwa pang'ono.

Tsopano ku Aroma 8:14 Paulo akuti:

Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu.

Kodi ana a Mulungu enieni ndi ati? Iwo omwe kawirikawiri amatsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Iyi ndi njira ina yolowa m'malo mosunga chilamulo. Mungathe kusunga ndondomeko ya malamulo kapena mungathe kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera, koma simungachite zonse.

Pali chitsanzo chomwe ndimagwiritsa ntchito chomwe chimabwera mu malingaliro anga. Ndiganiza ndichigwiritse ntchito kuti izi zimveke bwino. Pali mnyamata uyu, wangomaliza maphunziro a ku Baibulo sukulu. Wapeza digiri ya maphunziro a Mau a Mulungu, ndi wamphamvu ndi wathanzi, ndipo ayenera kupeza njira kupita mtsogolo kuchokera pa malo ena kukafika kwina. Mulungu amulankhula iye, "Tsopano uli ndi zinthu ziwiri zakuti usankhepo chimodzi. Ungathe kugwiritsa ntchito mapu kapena ungathe kudzipezeketsa kwa munthu wokutsogolera." Mnyamata uyu ndi kunena kuti, "ndine wodziwa bwino, ndiri ndi digiri ya maphunziro a Baibulo. Ndimadziwa kuwerenga mapu. Nditenga map, sindisowa

wonditsogolera.” Pomwe anyamuka, dzuwa likuwala, mbalame zikuimba, koma pakupita masiku atatu kutada. Ndipo pakati pa usiku, ali mu nkhalango, ali pafupi ndi chiphedi ndipo sakudziwa kuti kodi wayang’ana ku mpoto, kumadzulo, kumwera kapena kum’mawa. Liu lomveka chapansi limuuza iye, “Kodi ndingathe kukuthandiza.” Kodi mukudziwa yemwe iye ali? Mzimu Woyera, munthu wotitsogolera. Kotero anena, “Mzimu Woyera ndikufunani kwambiri?” Mzimu Woyera ndikumuturutsa iye pamalo pomwe ali ndipo ayambanso ulendo pa mseu.

Ndipo patapita kanthawi anenanso kwa iye mwini, “mu kudziwa, ndiganiza ndinapusa pang’ono. Ndikadakwaniritsa popanda thandizo lina liri lonse. Sindinayenera ine kuti ndipanikizike”. Ayang’ana yang’ana ndipo womutsogolera uja palibe. Ali yekha. “ndingathe kukwanitsa”.

Patapita masiku ena atatu ali mkatikati mwa malo a lowe. Mwendo uliwonse womwe aponda ukumatitimira mozama ndipo akulephera kuturuka. Mau a pansi amulankhulanso iye, “mwinatu ukundisowa tsopano,” “Oh, Mzimu Woyera chonde ndithandizeni! Ndinu nokha amene munganditurutse pano.” Ndipo kenaka apitirira ndi Mzimu Woyera pa njira yopita komwe amapita. Ndipo kenaka anena kwa Mzimu Woyera, kwa womutsogolera, “mukudziwa, ndiri ndi mapu ofotokoza bwino kwambiri. Kapena ndigawane nanu mapuwa.” Womutsogolera amuuza, “zikomo kwambiri koma ine sindisowa mapu. Ndikudziwa njira. Pambali pa ichi, ndine amene ndinapanga mapuwa.

Mukuona uthengawo? Zidzatitengera nthawi yaitali bwanji kuti tizindikire kuti sitingachite pa ife tokha? Si ntchito zathu zabwino, si kusunga malamulo kwathu, ndi Mzimu Woyera, Mzimu wa chisomo. Pakuti onse amene kawirikawiri atsogozedwa ndi Mzimu Woyera, amenewo ali ana a Mulungu.

Ndipo kenaka ku Agalatiya 5 Paulo akubwereranso ku mutu uwu. Ndifuna ndikuuzeni mutu uwu ndi umodzi wa mitu yaikulu mu Chipangano Chatsopano. Wina aliyense yemwe sanagwiritse ntchito mutu uwu ali mu malo a pakati pa m’dima ndi kuwala. Ndiganiza ndi pomwe akhristu ambiri amakhala, amakhala m’moyo wa pakati pa m’dima ndi kuwala, pakati pa chisomo ndi chilamulo, ndipo sadziwa kuti chenicheni ndi chiti ndiponso sadziwa kudzipezekeretsa okha ku chisomo cha Mulungu. Pa Agalatiya 5:18 Paulo akuti:

Ngati Mzimu akutsogolerani, simuli omvera lamulo.

Analankhula m’mbuyomo kuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu. Kotero, muli ndi chisankho mungathe kukhala ndi moyo monga Mwana wa Mulungu, tsogozedwani ndi Mzimu Woyera kapena, mungathe kutembenukira m’mbuyo mwanu kwa Mzimu Woyera ndi kuyesa kusunga lamulo. Koma simungathe kuphatikiza zonse ziwiri. Ichi ndi cholinga chomwe ine ndikuyesera kulankhula kwa inu. Apa ndi pomwe anthu amapezekera pakati pa mdima ndi kuwala. Akudalira mwatheka chisomo ndi theka malamulo awo ochepa omwe iwo akuyesetsa kusunga.

Chonde mvetsetsani sindikunena kuti ndi polakwika kusunga malamulo. Chomwe ndikunena ndi choti kusunga malamulo sikupangitsa muthu kukhala wolungama. Kodi mwachilandira ichi? Ndiganiza ndichinenenso. Kusunga malamulo sikungakupangitseni kukhala wolungama.

Ambiri a inu muli a mpingo kapena chipembedzo china chake, ndipo chiri ndi malamulo. Ndiganiza kuti ngati inu muli gulu limeneli muyenera kusunga malamulowo. Ngati simungasunge malamulo ndiye kuti musakhale a gululo. Koma, kusunga malamulo sikumakupangitsani kukhala wolungama. Zoona zake ndicho chimene chimayambitsa kwambiri mipatuko mu thupi la Khristu chifukwa magulu ambiri a chipembedzo ali nao malamulo awo, Baptist ali ndi ena, a Seventh Day Adventist alinso ndi ena, ma Pentecostal ali ndi ena, ndi enanso ao. Anthu ambiri mu magulu amenewa amaganiza kuti kusunga malamulo ndiko kumawapangitsa kukhala wolungama. Ndipo kenaka amayang'ana omwe ali ndi malamulo osiyana ndi kunena: kuti, chabwino, awo sali olungama kwenikweni chifukwa sakusunga malamulo athu." Ndiye mukuona chomwe chilamulo chimachita. Chimagawa thupi la Khristu.

A Baptist ali omasuka kusunga malamulo ao, ngati ali ogwirizana ndi Malemba. A Pentecostal chimodzimodzi. A Katorika, ngati ali ogwirizana ndi Malemba. Koma kumbukirani kuti palibe m'modzi wa iwo yemwe amayesedwa olungama mwa kusunga malamulo ao. Amayesedwa olungama ndi chikhulupiriro.

Vuto ndi lakuti ngati tikhazika pa malamulo tidzakhoza kuphonya pa chikhulupiriro ndipo tidzapezeka tonse mu malo a pakati pa kuwala ndi mdima. Kapena, monga mnyamata uja yemwe adaganiza kuti akadakhoza kukwaniritsa pogwiritsa ntchito mapu anapezeka mu lowe. Ena a inu mukudziwa momwe zikhalira kupezeka mu lowe. Zoona zake, ena a inu mulipano lero chifukwa munaturuka mu lowe ndi kuzindikira kuti musowa Mzimu Woyera. Amen? Amen.

Tsopano ndifuna ndilankhule mfundo ina yodzidzimutsa. Sindikadayerekeza kuinena kukadakhala kuti Paulo sadailankhule poyamba. Mudzaipeza ku Aroma 7. Ndikuuzani, Aroma ndi bukhu lodabwitsa. Ndinali mphunzitsi wa ukadaulo wa kuganiza bwino (Filosofe) ndisanatembenuke mtima kukhala Mkhristu. Ndimakondweretsedwa kwambiri ndi ukadaulo wakuganiza bwino (filosofe), ndipo ndikaganiza kuti ukadaulo wa kuganiza bwino ndi chinthu chodabwitsa ziri ngati komputa. Ngati mungaipatse nkhani yabwino komputa mudzapeza zotsatira zabwino. Koma ngati mungaipatse nkhani yoipa mudzapeza zotsatira zoipa. Kuganiza bwino sikumakupatsani mayankho, ukadaulo wa kuganiza bwino umangokuthandizani kudziwa ngati kumalizitsa kwanu kuli kolondola. Ndipo kotero, ndimakhoza kunena ine ndekha pa zinthu zonse zomwe ndinawerengapo, Baibulo ndilo bukhu lomwe liri bukhu la ukadaulo wa kuganiza. Pandekha ine sindimamva kuti ndiri pa kuganiza mwa ukadaulo, chifukwa ndimakhulupirira Baibulo. Umo ndi momwe mtima uliri. Ndikaganizira kuti inu, kuti musamadzione akuganiza moperewera. Angathe kukunenani muli ngati chinthu chomwe chiri chofunika kwambiri. Chabwino. Khalani wa chinthu chofunika kwambiri, chimene chiri. Makamaka, chimagwiritsidwa ntchito chomwe chimadzutsa zomva imva za moyo motsutsana nanu. Anthu omwe amalankhula za kukhala wa paphata sanafotokoze chomwe kukhala phata chiri. Pali mau ambiri omwe anthu amagwiritsa ntchito pakungofuna kuipitsa anthu ena koma samamasulira iwo. Musachite mantha kutchulidwa wa pa phata. Nthawi ina munthu wina akadzakutchulani inu choncho, "chonde, tandiuzani chomwe mutanthauza kuti wa paphata?

Chabwino, tsopano tikubwera ku mfundo yodzidzimutsa ya Paulo ku Aroma 7. Pomwe mupitabe chitsogolo ndi iye ndi momwe iye amatidzidzimutsa kwambiri. Aroma 7:4 ndi otsatira:

Chotero abale anga, inunso munayesedwa akufa ku chilamulo ndi thupi la Khristu, kuti mukakhale ake awina, ndiye amene anaukitsidwa kwa akufa, kuti ife tim'balire Mulungu zipatso.

Paulo akulankhula nthawi ina kamodzi ngati mu Yuda wa chipembedzo munakwatiwa ndi chilamulo. Ndipo kuti inu muchoke ku chilamulo ndi kuti mukwatiwe kwa wina chikadakhala chigololo, chigololo cha uzimu, pokhapokha mutapeza kuti chilamulo chinafa. Koma kudzera mu imfa ya Yesu pa mtanda chilamulo chinaphedwa kodi mukumvetsa?

Ili ndi vuto lalikulu la a Yuda ambiri. Amaona kuti ngati sangayesere kusunga chilamulo ndipo makamaka sachita zambiri za ichi, amakhala osakhulupirika kwa amuna ao. Payenera kukhala vumbulutso lakuti chilamulo chinaphedwa mwa Yesu kuti angathe tsopano kukwatiwa ndi wina, Messiah wouka kwa akufa. Ndi kudzera mwa iye (tonse) iwo ndi ife tithe kubereka zipatso. Kodi mukumvetsa? Chipatso chimadza ndi kukumana. Chomwe talumikizana nacho ndi chomwe chimapangitsa mtundu wa chipatso chomwe tingabereke. Koma tilumikizana, mu umodzi ndi Khristu, pamenepo tidzabereka chipatso cha Mzimu.

Popitiriza, Paulo akuti:

Pakuti pamene tinali mthupi, zilakolako za machimo, zomwe tinali nazo mwa chilamulo, zinali kuchita mziwalo zathu, kuti zibalire imfa zipatso.

Iyi ndi mfundo yodabwitsa, sichoncho? Zilako lako za machimo, zomwe tinali nazo mwa chilamulo, zinali kuchita mziwalo zathu, kuti zibalire imfa zipatso.

Iyi ndi mfundo yodabwitsa, sichoncho? Zilako lako za machimo zomwe zinali za chilamulo. Mwanjira ina, Paulo akuti, chilamulo chinatakasa zilakolako za uchimo. Mungathe kuzilandira izi?

Ndiroleni kuti ndikupatseni ndime ina ya pa 1 Akorinto 15:56. Iyi ndi imodzi ya mfundo mtengo wapatali.

Koma mbola ya imfa ndiyo uchimo; koma mphamvu ya uchimo ndiyo chilamulo.

Paulo akupitira kunena pa Aroma 7, akunena kuti palibe china chiri chonse cholakwika ndi chilamulo, chiri changwiro. Vuto liri mwa ife. Tawonani, Ndikufotokozereni motere: lamulo limagwira ntchito kuchokera kunja kwa munthu. Limati chita ichi, usachite ichi. Iwe umati "chabwino, ndichita ichi ndipo sindichita icho." Ndipo pakuchita ichi mukudalira mwa kuthekera kwanu. Iri ndiye vutolo chifukwa inu mulibe kuthekera kwa kuchita zabwino ndi kuleka kuchita zoipa. Koma taonani, chinthu chovuta cha thupi lathu ndicho kudzidalira ife tokha osafuna kudalira mwa Mulungu.

Tiyeni tibwere ku yeselo la m'munda mwa Edeni. Kodi mau okopa mtima omwe Satana anachigwiritsa ntchito ndi chiyani? "Mudzakhala ofanana ndi Mulungu. Palibe cholakwika muthu kuti ukhale ngati Mulungu. Nanga vuto linali chiyani? Adzakhala ofanana ndi Mulungu opanda kudalira Mulungu. Akadadalira pa chidziwitso cha zabwino ndi zoipa. Iri ndiye mutu wa vuto la munthu; ndilo muzu wa vuto la anthu a chipembedzo. Timafuna kufanana ndi Mulungu

koma sitifuna kudalira Mulungu. Pachimake pa uchimo ndiye kukana kudalira Mulungu. Uwu ndi uchimo muchimake.. Si chochita chapadera cha uchimo chomwe mumachita; ndi mtima wodzidalira omwe umatsekera chisomo cha Mulungu kunja kwa moyo wanu. Ndipo ichi chinthu chovutitsitsa, ndikhulupirira, kuti Mulungu ayenera kuchita ndi inu ndi ine, mu mtima uwu wa kudzilungamitsa nokha. "Ndingathe kuchita mwa ine ndekha, sindisowa Mulungu".

Monga momwe ndidziwira, ndipo iri ndi ganizo chabe, pali zolengedwa za mitundu iwiri zokha mu chilengedwe zomwe zidafuna kukhala mosadalira Mulungu. Choyamba ndi angero omwe adagwa amene adamtsatira Satana mu kuwukira kwake, ndi lachiwiri ndi mtundu wa anthu. Palibenso mu chilengedwe chomwe chimakhumba kukhala osadalira Mulungu. Mbalame sizikhumba kukhala osadalira Mulungu, zolengedwanso sizikhumba, nsomba sizikhumba nyenyezi sizikhumba…..zonse ndi zokondwa kudalira Mulungu. Koma inu ndi ine, chifukwa cha kugwa ndi chikhalidwe cha umunthu, tinalandira cholowa chavuto iri; sitikonda kudalira pa Mulungu. Timakonda kutha kunena, "Ndachita ichi mwa ine ndekha, sindisowa Mulungu."

Okondedwa abwenzi, musowa Mulungu mu njira yovutitsa ndipo musowa Mulungu kwambiri pomwe inu muganiza kuti simukumusowa. Ndipo ngati mungafufuze zochitika mu moyo wanu wa chikhristu ndiganiza mudzapeza kuti vuto liri lonse lomwe mwakumana nalo inu linaturuka mwa kufuna kuchita ichi popanda Mulungu, linaturuka kuchoka mu kukana kudalira pa chisomo cha Mulungu.

Rute anali mu chipatala zaka zingapo zapitazo kuyembekezera kuti apangidwe opareshoni. Anali ofooka kwambiri, ankafuna kuwerenga Baibulo lake koma sakadatha. Sisitere wamkulu, chinali chipatala cha Katolika Zotsatira zake ndi zokuti ku Amereka, atati ndisankhe chipatala, ndikhoza cha Katolika chifukwa palibe chifundo ngakhale pang'ono kumeneko. Chilipo pang'ono mu zipatala zina. Izi zikhoza kuti sizoona ku New Zealand, iyi ndi ndemanga chabe. Koma momwemobe , Rute anali ndi Baibulo lake koma anali ofooka kuti sangathe kuliwerenga. Sisitereyu wokondedwayu anati, "koma ufuna kuti ine ndiwerenge chiyani? Rute anati, "Afilipo 2" Sisitere anati, "chabwino, iri ndi lemba lomwe ndinakhazikitsidwira Sisitere" kotero anagwirizana.

Ndipo kenaka Sisitere uyu anafotokoza china chomwe chidachitika. Adali ku msonkhano wa ma Sisitere pomwe wolalikira adali Bambo wa nsembe (wa gulu lina lomwe ali ndi malamulo okhwima) wa ndondomeko ya Trappists. Awa Saloledwa kuyankhula akakhala kwawo (kumalo) yomwe akhala. Ali ndi chowinda/chilumbiro cha kusankhula. Koma mwa kamodzi kamodzi pomwe aloledwa kuturuka, pamenepo amaloledwa kuphunzitsa anthu zomwe aphunzitsi mu ukachete wao. Ndipo kotero, Bambo wa Trappist uyu amaphunzitsa ma Sisitere a chi Katorika awa ndipo ichi ndi chomwe adanena, ndipo sisitere adafotokozera Rute. Ichi chinandidalitsa ine kwambiri chifukwa ndinaona kuti ngati Mulungu afuna kuti china chake chidziwike, chimadziwika! Uyu ndi bambo yemwe sakuloledwa kuti alankhule, kuphunzitsa gulu laling'ono la ma Sisitere a chi Katorika omwe anali gulu pa iwo okha. Koma, uthenga uwu unandipeza ndipo ndinauika pa tepi kambiri mbiri ndipo wafikiranso dziko lapansi! Yemwe adapanga dongosolo iri ndani? Siwinanso koma Mulungu momwemobe ichi ndi chomwe wansembeyu wa Trappist analankhula kwa ma Sisitere awa.

Pempherani kukhala ndi chikhumbo chakusatamandidwa, wosadzidalira, ndi wosakhala olamulira

Kodi mungapemphere choncho?

Zimatengera kuchitapo kanthu pang'ono, sichoncho? Ndinaganiza ichi kwa nthawi yaitali. Chabwino, osati kuti nditamandidwe, ndiribe vuto lalikulu pa ichi osankha odzidalira, ndinazindikira kuti kudzidalira ndi kulakwitsa. Kukhala wotetezedwa osati kukhala otetezedwa – ndikonze ichi. Osatamandidwa, osatetezedwa, osakhala olamulira. Chabwino, ndi ziwiri zomalizira zomwe zimandisowetsa mtendere. Kodi ndingakhumbedi kukhala wopanda chitetezo? Chabwino, inde, chitetezo changa chiri mwa Mulungu. Koma ilankhula za kusakhala odzidalira, kusakhala olamula, pepani, ndi zovutitsitsa kwa ine. Kodi ndimakhumbadi kukhala wolamulira? Mu mau ena, kodi ndikufunitsitsadi kuti Mulungu alamulire? Iyi ndiye nkhaniyo. Ndicho chisomo, pomwe Mulungu akulamula.

Ndikuuzani, ndikudalitsa Sisitere uyu, ndiyembekeza akadali ndi moyo. Ndimuyamika chifukwa cha chomwe anaonjezera kudzera kwa Rute ku malingaliro anga. Taonani, ndimaona ichi ngati phata lalikulu la vuto la anthu, ndicho chokhumba kukhala wolamulira, kukhala wotetezedwa, ndi kukhala wodzidalira. Ndipo chofunika cha tchimo ndicho kukhala m'dziko lomwe lidalengedwa ndi Mulungu wachikondi ndi wanzeru zonse ndi kufuna kukhala wosadalira iye. Musandiuze, abale anga okondedwa ndi alongo, kuti simunakhalepo ndi vuto limenelo. Chifukwa, palibe m'modzi wa ife amene nthawi zonse adakhala okhutitsidwa kudalira Mulungu, kutola kuti Mulungu alamulire. Uku ndiko kuyenda kweni kweni kwa chikhulupiriro. Uku ndiko kuyenda kwa chisomo. Sitimachipeza mu ma ora ochepa. Zoona zake, zanditengera ine zaka zoposa 50 ndipo sindinafikepobe. Koma, ndiri pafupi kusiyana ndi momwe ndinaliri, ndiloleni ndikulimbitseni ndi ichi.

Tsopano tiyeni tipitire. Chilamulo chimatakasa tchimo. Chifukwa chiyani? Chifukwa lamulo limati "ungathe kuchita. Pitiriza, uzidalire wekha zonse zomwe uyenera kuchita ndi kusunga malamulo awa" ndi limakuchenjerera kuti alowe mu kudzidalira wekha. Iyi ndi njira yomwe lamulo limatinyenga ife. Ndipo chonde ndiloleni ndinene kuti palibe cholakwika ndi lamulo. Paulo akupitirira kunena mu mutu omwewo kuti lamulo ndi labwino, lamulo ndi la m'ngwiro, palibe cholakwika ndi lamulo. Vuto liri mwa ife. Mu chikhalidwe cha umunthu, tonse timakhumba kukhala odzidalira.

Ndiri ndi chitsimikizo kuti ambiri a inu munaonapo mwana. Ndimaona kuti kuyambira zaka ziwiri chikhumbo ichi chimayamba kuonekera. Munanena kwa mwana uyu wa ziwiri, "Bwera kuno". Ndipo amatembenuka nayamba kuyenda kupita kwina. Huh? Ndizoona? Iri ndilo khalidwe lakale la umunthu kudzionetsera lokha mwa ife. Lamulo ndi chizindikiritso cha Mulungu kubweretsa vuto limeneli poyera.

Mukuona, ngati mutapita kwa dotolo ndi kunena, "Dotolo, m'mimba mukundipweteka," sangangotenga bokosi losungira mankhala; ayesa kaye kuti apeze choyambitsa vuto la kuphweteka kwa m'mimba mwanumo. Apa tikuthandauza kuti, asanakulembereni chithandizo anayenera kupeza matenda anu. Umu ndi momwe Mulungu amachitira ndi ife. Samatipatsa

thandizo pokhapokha atapeza vuto lathu. Kenaka timadziwa kuti tisowa thandizo mu njira yovuta.

Kotero, tiyeni tipitirire tsopano ku Aroma 10:4

Pakuti Khristu ali chimaliziro cha lamulo, kulinga kuchilungamo cha lamulo, adzakhala nacho ndi moyo.

Kotero ngati mwakhala okhulupirika mwa Yesu Khristu, ndi mathero a chilamulo. Osati mathero a chilamulo mu zinthu zonse koma mathero a chilamulo chifukwa cha chilungamo? Monga mwa njira yopezera chilungamo ndi Mulungu, Khristu anathetsa chilamulo. Pomwe anafa, anachita zimenezo. Pomwe anauka kwa akufa anatipatsa ife njira ya tsopano yokhalira olungama ndi Mulungu yomwe siinali kusunga lamulo. Kotero, Khristu ndiye mathero a lamulo pa kulungamitsa. Sali mapeto a lamulo monga gawo la Mau a Mulungu kapena ngati gawo la mbiri ya Israel, kapena ngati chitsanzo cha njira yomwe Mulungu amachitira ndi anthu. Lamulo liripobe. Koma ngati njira yopezera chilungamo, imfa ya Yesu Khristu pa mtanda inathetseratu chilamulo.

Tsopano tiyeni kwa aka nthawi tione chitsanzo cha Akhristu aku Galatiya.

Agalatiya ndi kalata yotsangalatsa. Mukadakhala kuti muli ndi malingaliro a maphunziro a za Baibulo ndikadakufufuzani, “kodi ndi vuto lanji lomwe Paulo akuthana nalo kwa A Galatiya? Mungathe kunena kuti kusunga malamulo. Iri ndilo tanthauzo leni leni la maphunziro a Baibulo. Ambiri a makalata omwe Paulo amalembera mipingo, amayamba ndi mayamiko kwa Mulungu chifukwa cha zabwino zonse zomwe ziri mwa iwo. Ngakhale mpingo wa ku Korinto, komwe kunali munthu yemwe amagona ndi mkazi a bambo ake, ndipo komwe kunali kuledzera pa Gome la Ambuye, anayamba ndi kuyamikira kwake kwa Mulungu chifukwa cha chisomo cha Mulungu. Koma pomwe akuchita ndi AGalatiya alinso choncho ngati ndinganene, ananena mosanyengelera mwachindunji moti alibe nthawi yakuti ayamike Mulungu chifukwa cha chisomo chake. Kodi vuto lomwe linali ndi A Galatiya ndi lotani? Osati kuledzera, osati chiwerewere, koma chiyani? Kusunga malamulo. Paulo adaona vuto iri kuti ndi loopsya kwambiri ku ubwino wao koposa chiwerewere ndi kuledzera.

Tsopano chonde mvetsetsani sindikunena kuti Mulungu amakondwera ndi chiwerewere ndi kuledzera koma ndikunena kuti ndi vuto losavuta kuthana nalo kusiyana ndi kusunga malamulo, chifukwa kusunga malamulo ndi kochenjera koposa. Zimaoneka zabwino, timamva nacho bwino ichi, Kotero kuti ndi kovuta kuti timasulidwe ku ichi. Koma ichi ndi chomwe Paulo akunena ku Agalatiya 1:6:

Ndidziwa kuti mwa msanga motere mulikutunsika kwa iye amene anakuitanani m’chisomo cha Khristu, kutsata uthenga wabwino wina.

Onani, analibe chinthu china chabwino kunena. Anangoti, “ndadabwa kuti munatembenuka msanga motere.” Mu chiani? Mu kusunga lamulo, mu kusunga ndondomeko ya malamulo ndi kukhulupirira angathe kuyesedwa olungama ndi kutero.

Ndipo kenaka ku Agalatiya 3 akubwereranso ku mutu uwu kuyambira pa ndime 1.

Agalatiya opusa anakulodzani ndani?

Ndikumbukira zaka zapitazo ndinawerenga ndime imeneyi ndipo mwadzidzidzi ndinazindikira zoilankhula, A Khristu a Pentecostal kapena a karizimatiki akadakhoza kulodzedwa chifukwa palibe funso lakuti anali a karizimatiki. Zinakonza vuto lalikulu mu malingaliro anga inafotokozera kwa ine vuto lomwe lidabuka m'tchalichi yomwe ndinali mbusa. Sindipitamo mwatsatanetsatane koma ndidaona kuti mpingo wanga onse unalodzedwa ndi mkazi wa mbusa yemwe analipo ndisabwere ine yemwe adamusiya mwamuna wake ndi kukwatiwa ndi m'modzi wa atsogoleri… ndipo chinali chikuvutitsa kwambiri mwa iwo mu uzimu. Kotero ndiye ndingopereka ichi monga mukuthandizana. Ngati mulikukonza vuto lina lake lomwe simuli kulimvetsa, zikhoza kukhala kuti ndi vuto iri. Anthu omwe mukuchita nawo zinthu analodzedwa. Paulo akugwiritsa ntchito tanthauzo lomveka bwino iri. Zoona zake, liu la chi Griki lotanthauza kulodzedwa ndiro, "kukantha ndi diso". Akanthidwa ndi diso, afika pansi pa kuona kwa diso lomwe lowalodza iwo.

Ndinali ndi wansembe wa Orthdox wa chi Griki yemwe anabwera kwa ine zaka zapitazo yemwe adasanduka wa kalizimatiki. Anabwera kwa ine kuti ndimpempherere, anati, "ine ndalodzedwa, wina waika diso lake loipa pa ine sanaledzere ndipo amadziwa Baibulo lake. Sindifuna kutaya nthawi pa ichi koma ndifuna nditsegule kwa inu choona chakuti izi ndi zotheka. Zoona zake, mu malo ena ndi zotheka kuchitika.

Agalatiya opusa inu, anakulodzani ndani inu amene Khristu anaonetsedwa pamaso panu opachikidwa.

Paulo akuti "Ndinapereka kwa inu uthenga wa mtanda. Ndinaonetsa kwa inu Yesu wopachikidwa chifukwa cha machimo athu. Kodi mungakhale kuti munachotsedwa bwanji kuchokera ichi kupita ku maziko ena a chilungamo?"

Ichi chokha ndifuna ndiphunzire kuchoka kwa inu. Munalandira Mzimu (Mzimu Woyera) mwa ntchito za lamulo kapena mwa kumvera kwa chikhulupiriro?

Kodi munabatizidwa mwa Mzimu Woyera chifukwa munasunga malamulo kapena chifukwa munamva uthenga ndi kuulandira ndi chikhulupiriro?

Ndiroleni ndikufunseni funso iri. Kodi alipo pano nthawi ino yemwe anabatizidwa mwa Mzimu Woyera pa chifukwa cha kusunga malamulo? Yankho ndi lakuti palibe wina aliyense. Tiyenera kudziwa ichi. Sitinapulumutsidwe pa kusunga malamulo. Sitinalandire ubatizo wa Mzimu Woyera pa kusunga malamulo. Tinazilandira izi, monga Paulo akunena mwa kumvera kwa chikhulupiriro. Tinaphatikiza ndi chikhulupiriro uthenga womwe tinamva, tinaulandira ndipo tinaulandira.

Ndipo kenaka akuti:

Kodi ndinu opusa chotere, omwe munayamba ndi Mzimu (Mzimu Woyera) tsopano mukupangidwa kukhala wangwiro ndi thupi?

Zikaikidwa motero ndi kupusa, sichoncho? Ngati musowa Mzimu Woyera kukuyambitsani pa njira ya chilungamo, kodi mungasiye bwanji kudalira pa Mzimu Woyera? Kodi mungadalire bwanji pa m'ndandanda wanu waung'ono wa malamulo. Koma mukuona, izi ndi zenizeni zochitika.

Paulo akupitirira pa ndime ya 10.

Pakuti onse amene atama ntchito za lamulo liwakhalira temberero, pakuti kwalembedwa, Wotembereredwa ali yense wosakhala m'zonse zolembedwa m'bukhu la chilamulo, kuzichita izi.

Ngati mungalungamitsidwe mwa kusunga lamulo muyenera kusunga lamulo lonse nthawi zonse. Ndipo ngati muyesa kusunga lamulo ndipo ndikusasunga lamulo lonse nthawi zonse, mumudza pa temberero lomwe lakhazikisidwa, "wotembereredwa ndi amene sasunga mau a lamulo nthawi zonse".

Ndi zotheka kuti okhulupirira a ma Pentecostal ndi ma Karizimatiki kukhala pansi pa temberero? Ndifuna kukuuzani kuti ndi zotheka ndithu. Zoona zake, ndikudziwa kuchokera ku zondichitikira. Mwachidule ndinali m'modzi wa gulu lina mu thupi la Khristu lomwe lidayambika ndi Mzimu Woyera, mwa umulungu, mu ntchito zomwe wina ali yense wa ife sanayembekezere. Mulungu anandilumikizitsa ndi alaliki ena atatu, onse omwe ali odziwika bwino. Inali ntchito ya mu uMulungu wake wa Mulungu. Tinayamba mu Mzimu koma tisanafike ndi chaka chomwe mmugwirizanowu tidapezeka tathera mu thupi. Ndipo zotsatira zake zinali zosakhala bwino nkomwe. Kotero, ndidziwa izi zimachitika. Mukuona yemwe izi zidamuchitikira. Mulungu, mwa chisomo chake, anandilutsamo ndiganiza kuti chifukwa chakuti ndidawerenga Baibulo ndi kulikhulupirira. Ndinaona vuto lomwe ndidagweramo. Koma ndifuna ndikuuzeni, abale ndi alongo wanga okondedwa, izi si zinthu zoomwe zidachitika kale basi, zikuchitikabe ngakhale masiku ano. Anthu omwe amayamba mu uzimu ndipo kenaka amayesa kudzipanga ndi chikhalidwe cha thupi amadzibweretsela thembelero.

Ndikuganiza pa ine mwini, ngati ndinganene motero, kuti gawo lalikulu la mpingo liri pansi pa themberero.

Ndiroleni kuti ndikupatseni lemba lina lomwe ndi Yeremiya 17:5:

Atero Ambuye Yehova, Wotembereredwa munthu amene akhulupirira munthu, natama mkono wa nyama, nuchoka kwa Yehova mtima wake.

Tsopano, chifukwa ikunena kuti mtima wake umachoka kwa Yehova ndi zomveka bwino kuti munthu wotero adali ndi chiyanjano ndi Yehova. Koma atapeza ubale umenewu anayamba kenaka kudalira munthu, mwa iye mwini, ndipo mtima wake unachoka kwa Ambuye.

Ndikuona kuti ndi zomwe zidachitika kwa mipingo ya chikhristu yambiri yovomereza Khristu. Sindipereka maina ena ali wonse koma yambiri mwa mipingo yodziwika bwino kapena magulu a mipingo yomwe tikudziwa inayamba kudzera mukuchitachita kwa mphamvu ya Mulungu ndi ya Mzimu wa Mulungu, mwa chisomo cha Mulungu. Sakadakhoza kufikira pa china chiri chonse pambali pa ichi. Koma ndi angati a iyo lero omwe akupitirirabe mu chisomo cha Mulungu. Ndingathe kunena kuti ochepa. Kotero adzibweretsa okha pansi pa temberero lomwe lalengezedwa mu Yeremiya 17:5.

Wotembereredwa munthu amene akhulupirira munthu, natama mkono wanyama.

Ndiroleni ndifotokozere ichi kuchokera pa zomwe zidandichitikira. Rute ndi ine tidaganiza kuti tigulitse nyumba yathu mu Yerusalemu ndipo tinapita kwa omwe amagulitsira anthu nyumba, ndipo anati, "ndi nyumba yokongola, muigulitsa mwa changu uwu ndiye mtengo wake. Kwa miyezi 14 siinagulitsidwe. Sitinamvetsetse. Koma ndinali kumapemphero ku tchalichi mpingo wa Khristu, mpingo womwe timapemphera ku Yerusalemu, ndipo woyang'anira mpingo anati, "ndikuyenera ndipemphere ndi munthu yemwe amadziwa kumasula kuchoka ku mizimu (yonyansa) si oyang'anira mipingo onse omwe amalankhula choncho, koma uyu amalankhula. Ndi chifukwa chake timamukonda. Kotero ndinaganiza kuti ndipite ndikamuthandize. Ndinapita ku gawo iri ndipo munthu uyu anali wa mishoni wochokera ku Africa yemwe adafika ali pansi pa tembererolo, mu nthawi yomweyo. Ndifuna ndikuuzeni popanda kufotokoza, temberero linalengezedwa ndi Bishopu wakuda wa ku Africa. Anali pafupi kufa. Tinamutumikira ndipo anamasulidwa ku mitundu ingapo ya mizimu yoipa ndipo kenaka tinayamba kulimbana ndi mtima wake mokhudzana ndi moyo. Ndinamuuza, "Ukudziwa, zikuoneka kwa ine ngati kuti ukudzidalira kwambiri mwa iwe wekha. Simukudalira kwathunthu mwa chisomo cha Mulungu." Ndinanena," Ndi zoona, ndikudzidalira. "ndipo ndinavomereza ichi, ndinalapa ndi kudzimasula ndekha kuchoka ku temberero. Titamaliza msonkhano, ndinayendetsa galimoto yathu kupita ku nyumba yathu yatsopano komwe timakhala. Ndipo tiri panja tinakumana ndi wogulitsa nyumba yemwe anati, "ndimafuna ndisndiwonetse nyumba yanu kwa anthu omwe ndiri nawo amene akufuna kugula nyuma," Pasanathe masabata awiri nyumba inagulitsidwa. Mwaona? Nthawi yomwe ndinamasuka ku temberero Mulungu anakhoza kuyenda m'malo mwanga.

Ndikuona ena a inu mukulandira uthengawu. Chabwino.

Tiyeni tipitirire mtsogolo, pomwe tinali. Ndinene ndemanga zingapo mokhudzana ndi phunziro iri ndipo kenaka ndibwere ku zabwino. Ndanena kale ichi koma ndichibwereza, lamulo limagwira ntchito kuchokera kunja kutisiya ife mu kuthekera kwathu. Chisomo chimagwira ntchito kuchokera mkati kupereka kuthekela kwa uzimu. Tingathe kuchita izi mwa chisomo.

Ku Levitiko 11:44 ndi 1 Petro 1:16 tiri ndi lamulo lakuti "khalani oyera", iri ndi lamulo lochokera kwa Mulungu. Koma ngati muwerenga ku Levitiko 11, imafika ku mapeto kwa gulu la malamulo ofotokozedwa ndi kugawidwa bwino okhudza zomwe mungathe kudya ndi zakuti musadye. Kulumikizana kwa ichi ndi kwakuti ngati mungakhale oyera muyenera kusunga gulu la malamulo onsewo. Koma ku 1 Petro 1:16 sirinalumikizidwe ndi malamulo ena ali onse. Uthenga ndiwakuti "khalani oyera". Ndi uthenga wochokera kwa Yesu, "Ndiroleni ndikhazike chiyero changa mwa inu. "zosiyaniranatu. Osadaliranso pa mphamvu zathu koma kudalira pa chisomo cha Mulungu ndi Yesu kuchita zomwe sitingathe kuchita patokha. Muli ndi chisankho.

Tsopano tiri ndi nthawi yochepa kuti tione mbali yabwino ya ichi. Ndifuna ndiwerenge ku Aroma 8:3-4 ndipo muone chomwe chalembedwa kumeneko. Aroma 8:3 ndi 4.

Pakuti chimene chilamulo sichinathe kuchita, popeza chinafoka mwa thupi

Mukuona, palibe china chiri chonse cholakwika ndi chilamulo.

Mulungu anatumiza mwana wake wa Iye yekha m'chifanizo cha thupi la uchimo, ndi chifukwa cha uchimo natsutsa uchimo mthupi;

Kodi tsopano chabwinocho nchiyani?

…..kuti choikika chake cha chilamulo chikakwaniridwe mwa ife, amene sitiyendayenda monga mwa thupi, koma monga mwa Mzimu.

Ichi chikudzutsa chomwe anthu a ku America amachitcha, "funso la ma dollar chikwi". Kodi choyenereza cha chilungamo cha lamulo ndi chiyani? Kodi munayamba mwalingalilarapo izi? Ndingathe kukuyankhani ndi liu limodzi, si liu loipa. Ndi chikondi. Chikondi ndicho choyenereza cha lamulo cha chilungamo ndipo ndikuonetsani inu ichi mwachangu kudzera mu malemba angapo ndipo ndipo kenaka timaliza. Ku Mateyu 22 Yesu anafunsidwa ndi wa chimalamulo – mukudziwa kuti malingaliro ake anali a wachilamulo – mu ndime 35:

Ndipo m'modzi wa iwo, mphunzitsi wa chilamulo, anafunsa kumuyesa iye, nati, "Mphunzitsi, lamulo lalikulu ndi liti la mchilamulo?

Funso la chindunji ndipo Yesu anayankha nthawi yomweyo yankho la chindunji:

Ndipo Yesu anati, "Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako onse, ndi nzeru zako zonse. Iri ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba. Ndipo lachiwiri lolingana nalo ndiri, uzikonda mzako monga udzikonda iwe mwini.

Kodi liu la mtungulo ndi chiani? Chikondi. Chikondi pa Mulungu, chikondi pa anzathu. Ndipo kenaka Yesu anaikira ndemanga, "Pa malamulo awa awiri mpokolowelekerapo chilamulo chonse ndi aneneri."

Tsopano ngati tiri kumva kutentha, zomwe ine ndikumva, ndipo ndinafuna kuvula Jekete yanga ndi kuipachika ndikadasowa chikhomo (msumali) kuti ndipachikepo. Ndipo chikhomocho chinayenera kukhalapo kale ndisanapachikepo Jekete yanga. Malamulo ndi zikhomo zomwe chilamulo chonse ndi aneneri zimapachikidwapo. Mu kunena kwina, pomwe mwawerenga chilamulo chonse ndi aneneri, chomwe chiri kunena ndi chakuti kondani Mulungu, mnansi wanu. Ichi ndicho choyenereza chachilungamo cha chilamulo.

Ndipo kenaka ku Aroma 13:8 ndi zotsatira Paulo akuti:

Musakhale ndi mangawa kwa munthu ali yense, koma kukondana ndiko; pakuti iye amene akondana ndi mzake wakwaniritsa lamulo.

Ndimakhulupirira pa kukhala opanda ngongole, koma pali ngongole imodzi yomwe singaturukemo, ndiyo iti? Kukonda a khristu anzanga, kukonda anthu anzanga. Ndiri ndi ngongole, sindingaturukemo mu ngongole iyi.

Paulo akupitirira kunena:

Pakuti iri, "Usachite chigololo, Usaphe, Usabe, Usasirire, ndipo chingakhale lamulo lina liri lonse limangika pamodzi mau amenewa, kuti uzikonda mzako monga udzikonda iwe wekha. Chikondano sichichitira mzake choipa, chotero chikondano chiri chokwaniritsa lamulo.

Ndi zomveka bwino, sichoncho?

Ndipo kenaka ku Agalatiya 5:14 Ndipo zodabwitsa momwe Aroma ndi Agalatiya (amachitira limodzi) akhalira mofanana. Agalatiya 5:14.

Pakuti mau amodzi (chilamulo chonse chikwaniritsidwa mu mau amodzi) akwaniritsa chilamulo chonse ndiwo, "udzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini.

Ndipo kupitirira patsogolo pang'ono, pobwerera m'mbuyo ku Agalatiya 5:6 Baibulo likuti:

Pakuti mwa Khristu Yesu kapena m'dulidwe kapena kusadulidwa kulibe mphamvu; komatu chikhulupiriro chakuchititsa mwa chikondi.

Kodi chikhulupiriro chimagwira ntchito bwanji tanenani ? kudzera mu Chikondi

Mu bukhu la Yakobo likuti chikhulupiliro chopanda ntchito nchakufa. Ndiye chikhulupiriro chimagwira ntchito ndi chikondi. Ndiye zatibweretsa pa mfundo iyi: Chikulupiriro popanda chikondi, nchakufa. Ndi fundo yodzidzimutsa koma ndi zoona. Mungathe kukhala ndi chikhululupiriro chonse mungathe kunena koma ngati palibe chikondi mu moyo wanu ndi chikhulupiriro chakufa.

Ndipo kenaka tiwerenga ku 1 Timoteo 1:5 ndinaifotokozapo kale koma ndifuna ndiwerenge.

Koma chitsiriziro cha chilamulo ndicho chikondi chochokera mu mtima woyera ndi chikumbu mtima chokoma ndi chikhulupiriro chosanyenga; zimenezo, ena pozilambalala anapatukira kutsata mau opanda pake.

Tsopano mu Baibulo la chingerezi la New American Standard limati "chandamale cha chilangizo chathu ndi chikondi" pomwe ndinawerenga izi ndinadzifunsa ndekha kuti kodi ichi ndicho chandamaledi cha chilangizo? Kodi ndikufunadi kuti ndipange anthu achikondi? Ndaganiza za anthu ena omwe akhala pansi pa utumiki wanga ndipo ndinalibe chitsimikizo chifukwa kwakukulu ndine mphunzitsi ndipo mphunzitsi amapereka chidziwitso. Kodi mukudziwa zomwe chidziwitso chimachita? Chimadzikweza, chimapangitsa anthu kunyada. Ndinaphunzira kuti

ndiyenera kuyesetsa mwa kuthekera konse mu mphamvu zanga kuphunzitsa popanda kupanga anthu odzikweza. Koma ndiyenera kuyang'ana m'mbuyo kwa anthu ena omwe ndawaphunzitsa ndi kunena, "Chabwino, sindinagwire ntchito yabwino kwambiri." Chandamale cha chilangizo chathu ndi chikondi.

Ndipo kenaka Paulo akunena ngati musochera kuchoka pa cholinga chimenechi zonse zomwe mukuchita ndi kutsata mau opanda pake

Tiyeni kwa kanthawi tiringalire za mpingo monga momwe tiudziwira. Kutsata mau opanda pake kuli kwakukulu motani? Kodi ndi kulalikira kotani ndi kuphunzitsa ndi zochitika zomwe zimatulutsa chikondi chikondi? Zonse ndizo kungotaya mphamvu. Ziri zosathandiza. Abale ndi alongo, ngati muli mu utumiki wa mtundu uwu, ndifuna kukutsimikizirani inu, pangani kafukufuku wa zolinga zanu. Kodi cholinga chanu ndi chakuti mupange chiani? Ndipo chachiwiri, ngati mukufuna kupanga chikondi, kodi mukupangadi icho? Ndipo ngati simukufuna kupanga chikondi zolankhula zan zonse ndi mau opanda kanthu. Iyi ndi mfundo ya mtengo wapatali, sichoncho?

Mukuona, chilamulo chimagwira ntchito mwa ife kudzera mu mphamvu ya mantha koma Yesu amatipatsa mphamvu kudzera mu chikondi. Akuti, "ngati mukonda ine sungani malamulo anga". Mantha sabweretsa zotsatira ziri zonse. Pali zipembedzo zambiri zomwe zimalimbikitsa anthu mwa mantha ndipo zotsatira zake nzomvetsa chisoni kwambiri, kuphatikizapo ena a Khristu ovomeraza Khristu.

Kenaka ndifuna ndinene, ndipo tikufika kumapeto, kumvera kwa chikondi ndi kopitirira. Simuli angwiro mu chikondi, chabwino. Tiri limodzi, ine sindiri wa ngwiro mu chikondi. Koma sizitanthauza kuti sindiwerengedwa olungama chifukwa pokhapokha titapeza cholinga cha chikhulupiriro chathu ndi pomwe ziwerengedwa kwa ife chilungamo. Kodi mungathe kulandira ichi? Pokhapo pomwe mupitiriza kukhulupirira, chikhulupiriro chanu chimawerengedwa kwa inu chilungamo. Ichi chaperekedwa chitsanzo modabwitsa ndi mau a Yesu kwa Petro pa M'gonero wotsiriza, Anati, "Petro, udzandikana ine katatu "Petro anati," osati ine, sindingatero," "Ndipo kenaka Yesu anati, "Koma ndapemphera kuti chikhulupiriro chako chingazime." Kodi chinthu chofunika kwambiri ndi chiyani? Kuti chikhulupiriro chathu chingazime. Tingathe kulakwitsa mwambiri, tingathe ngakhale kuchimwa. Sitinafike, sitiri angwiro. Koma ife ngati titapitira kukhulupirira, chikhulupiriro chathu chidzawerengedwa kwa ife chilungamo mpaka titafika.

Ndipo ndiroleni kuti ndimalize ndi lemba limodzi lochokera kwa Yakobo, lomwe ndimalikonda. Ndiribe nthawi yakuti ndiike ndemanga pa mfundoyi koma ndiroleni ndingokupatsani inu.Yakobo 1:25

Koma iye wakupenyerera m'lamulo langwiro, ndilo laufulu, natero chipenyerere, ameneyo, posakhala wakumva wakuiwala, komatu wakuchita ntchito, adzakhala wodala mkuchita kwake.

Koma lamulo langwiro laufulu ndi chiyani mu mau amodzi? Chikondi, zoona. Mukuona, ngati mukondadi, mukondedi, muli munthu yekhayo waufulu kwathunthu chifukwa mungathe kukonda anthu nthawi zonse. Angathe kusakulabadira iwe, angathe kukuzunza, angathe kuyesa

ngakhale kukupha koma sangathe kukuletsani kuwakonda. Munthu yemwe chikakamizo chake ndi chikondi ndi munthu yekhayo waufulu kwathunthu mu dziko lapansi. Amen? Amen.

****